# Nkhani za kulowa ndi kutuluka m'dziko (Immigration) ndi Visa kwa Ozunzika kunkhanzaKugonana & Chipolowe

Ophunzira ochokera ku maiko akunja ndiponso ana asukulu ndi mafunso okhudza za kutuluka ndi kulowa m'dziko (immigration) ndi zitupa zawo zololedwa za visa, akulangizidwa kupeza thandizo kuchokera kwa loya wa immigration. Chikalata ichi ndi chipangizo cholongosola mbali zina za lamulo, koma si mlowa m'malo wa malangizo amalamulo.

**Ine ndakhala ndikuchitiridwa nkhanza, kodi immigration yanga ikukhudza ufulu wanga wogwiritsa ntchito zipangizo zapasukulu?**

Ayi. Pansi pa ulamuliro, ophunzira ndi ogwira nchito amene anachitidwa nkhanza kapena anapulumuka kunkhanza zokhudza kugonana ndi zapaubwenzi amalandira ufulu wofanana pansi pa Title IX ya 1972 Education Amendments (Title IX) ndi Violence Against Women Act (VAWA), posatengera kukhala ndi chilolezo cha immigration ndi Visa.

| | |
|---|---|
| Nkhani za zipangizo zamankhwala ndi uphungu pa sukulu chuma, komanso malo ogona omwe alipo, onani pa kangaude uyu: | https://1is2many.okstate.edu/ |
| Nkhani za ndondomeko ya makhalidwe a wophunzira, akupezeka pa kangaude uyu: | https://studentconduct.okstate.edu/code |

Koleji siidzakubwenzerani kapena kukusiyanitsani ndi ena chifukwa chochita lipoti mlandu.

**Kodi ndingakasume milandu monga munthu wolowa m'dziko (immigrant) wokhala ndi kalata ya chilolezo kapena wopanda kalata ya chilolezo?**

| | |
|---|---|
| Inde. Nkhani zoyankha zokhudza milandu yanu ya nkhanza zogonana, nkhanza zapanyumba, ziwawa za paubwenzi ndi kulondalonda zingapezeke mu Annual Security Report: | https://police.okstate.edu/annual-security-reports |

Mafunso okhudzana ndi kusuma milandu akhoza kutumizidwa kwa:

Oklahoma State University Police Department, OSUPD
104 USDA Building, Stillwater, Oklahoma 74078
405-564-6523
https://police.okstate.edu/
1is2many@okstate.edu

**Kodi pali ma visa ena ndi immigration zokhudza amilandu?**

Inde. A nkhanza zogonana, nkhanza zapanyumba, nkhanza zapaubwenzi ndi kulondalonda, pangakhalenso njira zina za visa, kuphatikizapo ma Visa a U ndi T. Kuti mudziwe zenizeni, yankhulani ndi loya wa immigration.

| U Visa | T Visa |
|---|---|
| Kwa iwo wokhudzidwa ndi nkhanza zovulazidwa kapena zosokoneza mutu chikwa cha mchitidwe wa upandu umene anakumana nawo, kuphatikizapo nkhanza za chiwerewere, nkhanza zapanyumba, kugwiriridwa, kufwambidwa, kapena milandu ina yofanana.<br>-Wochitiridwa nkhanza/osuma ayenera kukhala wothandiza kuchita zinthu zothana ndi mchitidwe wa nkhanza ndiponso ayenera kuthandiza kufufuza ndi / kapena kuyimba mlandu wa mchitidwe woipawo<br><br>-Kawirikawiri ndiyovomerezeka kwa zaka zinai<br>-Kuti mudziwe zambiri, funsani loya wa immigration, ndi kuwona:<br><br>http://www.uscis.gov/humanitarian/victims-human-trafficking-other-crimes/victims-criminal-activity-u-nonimmigrant-status/victims-criminal-activity-u-nonimmigrant-status | Kwa iwo wokhudzidwa ndi malonda ogulitsa anthu<br>-Akuyenera kugwirizana ndi mafunso omveka bwino kuchokera kwa azamalamulo akudzipereka mu kafukufuku kapena milandu ya yogulitsa anthu (pokhapokha ngati akulephera kutero chifukwa cha chilema kapena kusokonekera mutu), ndipo ayenera kukwanitsa kusonyeza kuti wozunzidwayo/wodandaulayu adzazunzika kwambiri zedi ngati achotsedwa m'dziko la United States<br>-Kawirikawiri ndiyovomerezeka kwa zaka zinayi<br>-Kuti mudziwe zambiri, funsani loya wa immigration, ndi kuwona:<br><br>http://www.uscis.gov/humanitarian/victims-human-trafficking-other-crimes/victims-human-trafficking-t-nonimmigrant-status |

**Kodi pali ofesi pa sukulu imene ingandiyankhe zina zambiri?**

, International Students & Scholars

250 Student Union, Stillwater, OK 74078
405-744-5459
https://lcl.okstate.edu/iss/
su-iss@okstate.edu

International Student ndi Scholar Services Office angathandize kupereka mawu othandiza okhudza za immigration. Dziwani kuti za mafunso okhudza kusintha kwa mavisa ena, kapena zisankho za malamulo zimene zimagwa kunja kwa ma standard visa a F-1 ndi J-1 awophunzira, kapena mavisa antchito opangidwa siponsa ndi mabwana, kaonaneni ndi loya wa immigration.

| Njira za Visa |
|---|

SUNY The State University of New York

| | |
|---|---|
| Ophunzira okhala ndi F-1 ndi J-1<br>• Njira za maphunziro ololedwa kuchepetsedwa chifukwa cha matenda otsimikizidwa ndi dokotala ovomerezeka wazamankhwala, dokotala wa dongosolo la machiritso limene limakhudzana ndi kupotokola kwa ziwalo monga molumikizana mafupa, kapena wachipatala ovomerezeka ophunzitsa za momwe anthu amaganizira<br>• Njira za, ndi zotsatira pa, kusiyira panjira maphunziro anu<br>• Zambiri zakubweleranso kukapitiriza maphunziro patapita nthawi, ngati ophunzira anasiyira panjira<br>• Njira ndi zotsatira chifukwa choperekeza banja lanu<br>• Zina zambiri za njira zosinthira visa.<br>• Zina zambiri za mavisa a U ndi T. (Onanani ndi loya ovomerezeka wa immigration)<br>• Onanani ndi loya ovomerezeka | H-1B, O-1, E-3, kapena ogwira ntchito a TN<br>• Njira za tchuthi chojomba kuntchito, ndi zotsatira za immigration yanu<br>• Njira ndi zotsatira chifukwa choperekeza okondeka anu<br>• Zambiri za njira zosinthira mavisa. Onanani ndi loya ovomerezeka wa immigration<br>• Zina zambiri za mavisa a U ndi T. (Onanani ndi loya ovomerezeka wa immigration)<br>• Onanani ndi loya ovomerezeka wa immigration<br>• Kudikilira chilolezo chokhala ku U.S. mpaka kalekale (green card siinavomerezedwe kaye)<br>• Chotsatira ukasiya kugwira ntchito imene mapepala ake okuyenerezani kukhalira m'dziko kwa muyaya anakupangirani ndi bwana wanu amene mumamugwirira ntchito;<br>• Onanani ndi loya ovomerezeka |

**Kodi loya wa immigration ndi ndani ndipo amachita chiyani?**

Maloya a immigration ndi owona zamalamulo ovomerezeka amene amaona za malamulo okhudza immigration. Amagwira ntchito ngati mkhala-pakati wa anthu ofuna thandizo, ndipo akhodza kuwaimira pamaso pa mabungwe a immigration, kukhoti ya immigration komanso kuyankha mafunso papepala okomera immigration. Loya akhodza kupereka malangizo ali onse ndipo akhodza kukamba za njira za immigration. Monga maloya onse, maloya a immigration ndiophunzira bwino ndipo amachita zofunikira, ndikusunga chinsisi cha zimene ayankhulana ndi anthu amene akuwathandiza kapena kuti akuwaimilira.

**Kodi loya wa immigration wam'deralo angapezeke kuti?**

| |
|---|
| U.S. Citizenship and Immigration Services (USCIS), bureau ya Department ya Homeland Security (DHS), imapereka masaiti awiri othandiza anthu kupeza oimira ovomerezeka aulere kapena otchipa:<br>USCIS: Pezani thandizo ku malo anu pa tsamba la kangaude uyu     USCIS: Pezani thandizo la za malamulo pa tsamba la kangaude |
| A bungwe loona pa kusuma kwa kulowa ndi kutuluka m'dziko [The Board of Immigration Appeals (BIA)] amapereka ndondomeke ya maloya wopereka thandizo kwa ulere kapena kwa ndalama yocepa cabe. |
| A bungwe la [The American Immigration Lawyers Association (AILA)] iwo amapereka thandizo yapa laini (online) imene itha kuthandiza wophunzira kuti apeze loya wofunikira pa nkhaniyi |
| A bungwe la [The American Bar Association] amapereka thandizo la komwe mutha kupeza loya m'boma lina lirilonse. |